

“Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.”

**Mmene
Tingamdziwire
Mulungu**

Mmene tingamdziwire Mulungu

Monga Abrahamu adali “bwenzi la Mulungu” mwa kugonjera kwake ndi kumvera Mulungu, inunso mukhoza kumdziwa Mulungu ndi Kulandira chifundo, mtendere ndi mdalitso wake. Kumdziwa Mulungu *mwakuginjera moona* kwa iye mchikhulupiroro ndi cho chinthu chofunikira kwambiri mmoyo wa munthu. Ndi chodabwitsa kuti Mulungu amadzionetsera yekha kwa iwo amene amfuna iye ndi mtima wawo wonse!

***Mukasiya* kuyenda njira zanu ndi *kugonjera kwa Mulungu moona*, Mzimu wake adzakhala mwa inu. Palibe Chimene chingadza-kulekanitseni ndi chikondi chake, Pamene *mukhulupirira* mma-lonjezano ake ndi kumtsatira mkumvera. Adzakhala Mulungu wanu ndipo inu mudzakhala chuma chake chopambana. Mudzapeza kuti adakugulani inu ndi mtengo waukulu, ndipo akufuna kuyanjanana nanutsopano ndi kunthawi zonse.**

Mumpemphe Mulungu kuti akupatseni chidziwitso mmene mukusanthula mdime izi za Mawu a Mulungu.

Ndime zonse za mkabuku aka zachokera mBaibulo: Chilamulo (Torah), Masalmo (Zabur) aneneri, ndi Uthenga wabwino (Injil).

... Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi; ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse.
—Deuteronomo 6.4, 5

Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwacabe; Iye analiumba akhalemo anthu; Ine ndine Yehova; ndipo palibenso wina.
—Yesaya 45.18

Kuti anthu onse a pa dziko lapansi akadziwe kuti Yehova ndiye Mulungu, palibe wina.
—1 Mafumu 8.60

Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli; ndipo ulemmerero wanga Ine sindidzapereka kwa wina, ngakhale kunditamanda kwa mafano osemedwa.
—Yesaya 42.8

Inu ndinu mboni zanga, ati Yehova, ... kuti mundidziwe, ndi kundikhulupirira Ine, ndi kuzindikira, kuti Ine ndine; ndisanakhale Ine, panalibe Mulungu wolenge-dwa, ngakhale pambuyo panga sipadzakhala wina. Ine, Inetu ndine Yehova; ndipo palibe Mpulumutsi, koma Ine ndekha. Yang'anani kwa Ine, mupulumutsidwe, inu malekezere onse a dziko; pakuti Ine ndine Mulungu, palibe wina.
—Yesaya 43.10, 11; 45.22

2 Mulungu ndi Wachifundo ndi Wokoma Mtima

Yehova ndiye wa nsoni zokoma ndi wacisomo, wosakwiya msanga, ndi wa cifundo cocuruka. Pakuti monga m'mwamba mutaliki-ra ndi dziko lapansi, motero cifundo cace cikulira iwo akumuopa Iye. —Masalmo 103.8, 11

Koma cifundo ca Yehova ndico coyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha kwa iwo akumuopa Iye.... Ndi kwa iwo akukumbukila malangizo ace kuwacita. —Masalmo 103.17, 18

Ndani Mulungu wofanana ndi Inu, wakukhululukira mphulupulu, ... popeza akondwera naco cifundo. —Mika 7.18

Cifukwa cakusathedwa ife ndi-

co cifundo ca Yehova, pakuti cisoni cace sicileka; cioneka catsopano m'mawa ndi m'mawa

—Maliro 3.22, 23

Angakhale aliritsa, koma adzacitira cisoni monga mwa kucuruka kwa zifundo zace. —Maliro 3.32

Pa wacifundo mukhala wacifundo —Masalmo 18.25

... Pakuti ndinadziwa kuti Inu ndinu Mulungu wacisomo ndi wozala cifundo, wolekerera ndi wokoma mtima mocuruka, ndi woleka coipaco. —Yona 4.2

Yamikani Yehova; pakuti Iye ndiye wabwino; pakuti cifundo cace ncosatha. —1 Mbiri 16.34

Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde, ndakukonda iwe ndi cikondi cosatha; cifukwa cace ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima. —Yeremiya 31.3

Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezero.

—Yeremiya 29.11

Ndakukondani, ati Yehova

—Malaki 1.2

Monga atate acitira ana ace cifundo, Yehova acitira cifundo iwo akumuopa Iye. —Masalmo 103.13

Taonani, ndinali ndi zowawa zazikuru, cifukwa ca mtendere wa-

nga; koma Inu (O Mulungu) mokonda moyo wanga, munaupulumutsa m'dzanja la cibvundi, pakuti mwaponya m'mbuyo mwanu macimo anga onse. —Yesaya 38.17

Ndipo ife tazindikira, ndipo takhulupirira cikondico Mulungu ali naco pa ife. . . . Tikonda ife, cifukwa anayamba Iye kutikonda.

—1 Yohane 4.16, 19

Yehova Mulungu wako ali pakati pako, wamphamvu wakupulumutsa; adzakondwera nawe ndi cimwemwe, adzakhala wopanda thamo m'cikondi cace; adzasekerera nawe ndi kuyimbirapo.

—Zefaniya 3.17

4 Chinthu chachikulu mmoyo ndi kumdziwa Mulungu

... Koma anthu akudziwa Mulungu wao adzalimbika mtima, nadzacita mwamphamvu.

—Danieli 11.32

Koma wakudzitamandira adzitamandire adzikweze umo, kuti ali wakuzindikira, ndi kundidziwa Ine, kuti ndine Yehova wakucita zokoma mtima, ciweruziro, ndi cilungamo m'dziko lapansi, pakuti m'menemo ndikondwerera, ati Yehova.

—Yeremiya 9.24

Odala iwo akusunga mboni zace, akumfuna ndi mtima wonse.

—Masalmo 119.2

... Ndaika pamaso panu moyo ndi imfa, mdalitso ndi temberero;

potero, sankhani moyo, kuti mukhale ndi moyo, inu ndi mbeu zanu; kukonda Yehova Mulungu wanu, kumvera mau ace, ndi kummatira Iye, pakuti Iye ndiye moyo wanu —Deuteronomo 30.19, 20

Pakuti ndikondwera naco cifu-ndo, si nsembe ai; ndi kumdziwa Mulungu koposa nsembe zopse-reza.

—Hoseya 6.6

Monga nswala ipuma wefuwefu kukhumba mitsinje; motero moyo wanga upuma wefuwefu kukhumba Inu, Mulungu. —Masalmo 42.1

Ndipo anati, Nkhope yanga idzamuka nawe, ndipo ndidzakupumuza.

—Eksodo 33.14

... Yehova ali nanu; mukakhala ndi Iye, mukamfuna Iye, mudzampeza; koma mukamsiya, adzakusiyani. —2 Mbiri 15.2

Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosaciritsika, ndani angathe kuudziwa? —Yeremiya 17.9

Iripo njira yooneka kwa mwamuna ngati yoongoka, koma matiriziro ace ndi njira za imfa. —Miyambo 16.25

Pakuti ngati Mulungu sanalekerera angelo adacimwawo, koma anawaponya kundende nawaika ku maenje a mdima, asungike akaweruzidwe. Ambuye adziwa kupulumutsa opembedza poyesedwa iwo, ndi kusunga osalungama ku-

fikira tsiku loweruza akalangidwe. —2 Petro 2.4, 9

Koma mukapanda kumvera mau a Yehova, ndi kupikisana ndi lamulo la Yehova, dzanja la Yehova lidzatsutsana nanu, monga linatsutsana ndi makolo anu.

—1 Samueli 12.15

Tsoka kwa ana opanduka, ati Yehova, amene atenga uphungu koma si pa Ine; ... kuti aonjezere cimo ndi cimo. —Yesaya 30.1

Ngati wina sakhala mwa Ine, watayika kunja monga nthambi, nafota; ndipo azisonkhanitsa nazitaya kumoto, nazitentha.

—Yohane 15.6

6 Kuti timdziwe Mulungu tiyenera kumfunafuna iye

Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.

—Yeremiya 29.13

Ukaifunafuna... ngati cuma cobisika; pompo udzazindikira... kumdziwadi Mulungu.

—Miyambo 2.4, 5

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu.

—Mateyu 7.7

Koma wopanda cikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi

kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye.

—Ahebri 11.6

Akundikonda ndiwakonda; akundifunafuna adzandipeza.

—Miyambo 8.17

Yehova akhalira wabwino omli-ndirira, ndi moyo womfunafuna.

—Maliro 3.25

Ndipo ndi mmodzi analenga mitundu yonse ya anthu,... kuti afunefune Mulungu, kapena akamfufuze ndi kumpeza, ngakhale sakhala patari ndi yense wa ife.

—Macitidwe a atumwi 17.26, 27

Koma ine ndikadafuna Mulungu, ndikadaikira mlandu wanga Mulungu.

—Yobu 5.8

... Pakuti Yehova Mulungu wanu ngwa cisomo ndi cifundo; sadzakuyang'anirani kumbali ngati mubwera kwa Iye. —2 Mbiri 30.9

Pakuti Inu, Ambuye, ndinu wabwino, ndi wokhulukira, ndi wa cifundo cocurukira onse akuitana Inu. —Masalmo 86.5

Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu. . . . —Yakobo 4.8

Yehova ali pafupi ndi onse akuitanira kwa Iye, onse akuitanira kwa Iye m'coonadi. —Masalmo 145.18

Tiyeni, tsono, tiweruzane, ati Yehova; ngakhale zoipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngati matalala;

ngakhale ziri zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkho-sa, woti mbu. —Yesaya 1.18

Inu nonse, inu akumva ludzu, idzani kumadzi; ndi osowa ndarama idzani inu mugule mudyé; inde idzani —Yesaya 55.1a

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. —Mateyu 11.28, 29

... Ndipo wakudza kwa Ine sindidzamtaya iye kunja. —Yohane 6.37

Mulungu ndi Woyera

Afanana ndi Inu ndani... Yehova? ... wolemekezedwa, woyera, woopsa pomyamika, wakucita zozizwa? —Eksodo 15.11

Palibe wina woyera ngati Yehova; palibe wina koma Inu nokha... —1 Samueli 2.2

Cifukwa cace mundimvere ine, eni nzeru inu, nkutali ndi Mulungu kucita coipa, ndi Wamphamvuyonse kucita cosalungama. —Yobu 34.10

... Woyera, Woyera, Woyera, Yehova wa makamu; dziko lonse lapansi ladzala ulemmerero wace. —Yesaya 6.3

Pakuti atero Iye amene ali wantari wotukulidwa, amene a-

khala mwacikhalire, amene dzinalace ndiye Woyera, Ndikhala m'malo atari ndi oyera... —Yesaya 57.15

Yehova ali wolungama m'njira zace zonse, ndi wacifundo m'nchito zace zonse. —Masalmo 145.17

... Palibe wabwino koma mmodzi, ndiye Mulungu. —Marko 10.18

Ndani adzakhala wosaopa ndi wosalemekeza dzina lanu Ambuye? Cifukwa Inu nokha muli woyera... —Cibvumbulutso 15.4

... Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, amene anali, amene ali, ndi amene alinkudza.

—Cibvumbulutso 4.8

Anthu a Mulungu ayenera kukhala Moyo Wa Chiyero 9

Ukhulupirira iwe kuti Mulungu ali mmodzi; ucita bwino; ziwanda zikhulupiranso, ndipo zinthunthumira. Koma ufuna kuzindikira kodi, munthu wopanda pace iwe, kuti cikhulupiriro copanda nchito ciri cabe?

Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudzinyenga nokha. —Yakobo 2.19, 20; 1.22

Iye wakunena kuti, Ndimdziwa Iye, koma wosasunga malamulo ace, ali wabodza, ndipo mwa iye mulibe coonadi. M'menemo aoneka ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi: yense wosacita cilungamo siali wocokera mwa Mulungu; ndi

iye wosakonda mbale wace.

—1 Yohane 2.4; 3.10

Njira ya oipa inyansa Yehova; koma akonda wolondola cilungamo.

—Miyambo 15.9

Londolani mtendere ndi anthu onse, ndi ciyeretso cimene, akapanda ici, palibe mmodzi adzaona Ambuye.

—Ahebri 12.14

Komatu monga Iye wakuitana inu ali woyera mtima, khalani inunso oyera mtima m'makhali-dwe anu onse.

—1 Petro 1.15

Funani cokoma, si coipa ai; kuti mukhale ndi moyo; motero Yehova Mulungu wa makamuna adzakhala ndi inu, monga munena.

—Amosi 5.14

... Ndipo Yehova afunanji nawe koma kuti ucite colungama, ndi kukonda cifundo ndi kuyenda modzicepetsa ndi Mulungu wako?

—Mika 6.8

... Muzikhala oyera; pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu, ndine woyera.

—Levitiko 19.2

... Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu yako yonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mnansi wako monga iwe mwinini.

—Luka 10.27

Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zole-

mbedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru.

—Yoswa 1.8

Udziwa malamulo: Usaphe, Usacite cigololo, Usabe, Usacite umboni wakunama, Usanyenge, Lemekeza atate wako ndi amako.

—Marko 10.19

Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu . . .

—Aroma 12.2

... Khulupirirani Mulungu.

—Marko 11.22

... Kuti iye amene akonda Mulungu akondenso mbale wace.

—1 Yohane 4.21

Ziripo zinthu zisanu ndi cimodzi Mulungu azida; ngakhale zisanu ndi ziwiri zimnyansa: Maso akunyada, lilime lonama, ndi manja akupha anthu osacimwa; mtima woganizira ziwembu zoipa, mapazi akuthamangira mphulupulu mmangu mmangu; mboni yonama yonong'ona mabodza, ndi wopikisanitsa abale. —Miyambo 6.16-19

Pakuti Ine Yehova ndikonda ciweruziro, ndida cifwamba ndi coipa —Yesaya 61.8

Koma amantha, ndi osakhulupira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi acigololo, ndi olambira mafano, ndi onse a mabodza, colandira cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi

moto ndi sulfure; ndiyo imfa yaciwiri. —Cibvumbulutso 21.8

. . . Koma sungani mzimu wanu; ndipo asamcitire monyenga mkazi wa ubwana wace ndi mmodzi yense. Pakuti ndidana nako kuleka kumene, ati Yehova

—Malaki 2.15, 16

Ndipo musalingirira coipa m'mtima mwanu yense pa mnzace; nimusakonde lumbiro lonama; pakuti izi zonse ndidana nazo, ati Yehova. —Zekariya 8.17

Yehova ayesa wolungama mti: Koma moyo wace umuda woipa ndi iye wakukonda ciwawa. —Masalmo 11.5

12 Anthu amaperewera pa zofuna za Mulungu

Koma ndikudziwani inu, kuti mulibe cikondi ca Mulungu mwa inu nokha.
—Yohane 5.42

Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wacimwira onse.
—Yakobo 2.10

Ndipo ine ndinati, Tsoka kwa ine! cifukwa ndathedwa; cifukwa ndiri munthu wa milomo yonyansa, ndikhala pakati pa anthu a milomo yonyansa; cifukwa kuti maso anga aona Mfumu, Yehova wa makamu.
—Yesaya 6.5

Potero kwa iye amene adziwa kucita bwino, ndipo sacita, kwa iye kuli cimo.
—Yakobo 4.17

Monga kwalembedwa, palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi.
—Aroma 3.10

Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu.
—Aroma 3.23

... Yense wosacita cilungamo siali wocokera mwa Mulungu; ndi iye wosakonda mbale wace.
—1 Yohane 3.10

Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha
—Yesaya 53.6

... Akhoza ndani kuima pamaso pa Yehova, Mulungu Woyera uyu?
—1 Samueli 6.20

Pakuti ndiwacitira iwo umboni kuti ali ndi cangu ca kwa Mulungu, koma si monga mwa cidziwitso. Pakuti pakusadziwa cilungamo ca Mulungu, ndipo pofuna kukhazikitsa cilungamo ca iwo okha, iwo sanagonja ku cilungamo ca Mulungu. —Aroma 10.2, 3

Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati cobvala codetsedwa; ndipo ife tonse tifota monga tsamba, ndi zoiipa zathu zitiuluza monga mphepo. —Yesaya 64.6

Ndikanena kwa wolungama kuti adzakhala ndi moyo ndithu,

akatama cilungamo cace, akacita cosalungama, sizikumbukika zolungama zace ziri zonse; koma m'cosalungama cace anacicita momwemo adzafa. —Ezekieli 33.13

Ndipo iwo amene ali m'thupi sangathe kukondweretsa Mulungu. —Aroma 8.8

Cifukwa kuti pamaso pace pali-be munthu adzayesedwa wolungama ndi nchito za lamulo —Aroma 3.20

Si kuti tiri okwanira pa ife tokha, kuyesera kanthu monga mocokera mwa ife tokha; kukwanira kwathu kucokera kwa Mulungu. —2 Akorinto 3.5

Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anaci-mwa. —Aroma 5.12

Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa.

—Yakobo 1.15

Koma zoipa zanu zakulekani-tsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo macimo anu abisa nkhope yace kwa inu, kuti Iye sakumva.

—Yesaya 59.2

Wolimbikira cilungamo alandira moyo; koma wolondola zoipa adzipha yekha. —Miyambo 11.19

... Atero Mulungu, Mulakwiranji malamulo a Yehova kuli kosalemerera nako? Popeza mwasiya Yehova, Iye wasiyanso inu.

—2 Mbiri 24.20

Pakuti kupanduka kuli ngati cipapa ca kucita nyanga, ndi mtima waliuma uli ngati kupembedza milungu yacabe ndi maula. Popeza inu munakaniza mau a Yehova, Iyenso anakaniza inu

—1 Samueli 15.23

Moyo wocimwawo ndiwo udzafa

—Ezekieli 18.20

... Pakuti Inu mwatibisira nkhope yanu, ndipo mwatinyeketsa ndi zoipa zathu. —Yesaya 64.7

Mulungu ndiye Woweruza wolungama, ndiye Mulungu wakukwiya masiku onse. —Masalmo 7.11

Yehova ndiye wolekerera mkwiyo, koma wa mphamvu yaikuru; ndi wosamasula ndithu woparamula —Nahumu 1.3

Cifukwa ca izi zomwe ukudza mkwiyo wa Mulungu pa ana a kusamvera. —Akolose 3.6

Pakuti mkwiyo wa Mulungu, wocokera Kumwamba, uonekera pa cisapembedzo conse ndi cosalungama ca anthu, amene akanikiza

pansi coonadi m'cosalungama cao. —Aroma 1.18

Anadzala ndi zosalungama zonse, kuipa, kusirira, dumbo; odzala ndi kaduka, mbanda, ndeu, cinyengo, udani; akazitape, osinjirira, akumuda Mulungu, acipongwe, odzitama, amatukutuku, oyamba zoipa, osamvera akuru ao, opanda nzeru, osasunga mapangano, opanda cikondi ca cibadwidwe, opanda cifundo; amene ngakhale adziwa kuweruza kwace kwa Mulungu, kuti iwo amene acita zotere ayenera imfa, azicita iwo okha, ndiponso abvomerezana ndi iwo akuzicita. —Aroma 1.29-32

... Kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, ciweruziro.
—Ahebri 9.27

Kugwa m'manja a Mulungu wamoyo nkoopso. —Ahebri 10.31

Ndipo ndinena kwa inu, kuti mau onse opanda pace, amene anthu adzalankhula, adzawawerengera mlandu wace tsiku la kuweruza. —Mateyu 12.36

Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo buku lina linatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao. Ndipo ngati munthu sana-

pezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto. —Cibvumbulutso 20.12, 15

Pakuti Mulungu adzanena mlandu wa zocita zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale zabwino ngakhale zoipa. —Mlaliki 12.14

Padzatero pa cimariziro ca nthawi ya pansi pano: angelo adzaturuka, nadzawasankhula oipa pakati pa abwino, nadzawataya m'ng'anjo yamoto; komweko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano. —Mateyu 13.49, 50

... Adzaweruza dziko lokhalamo anthu ndi cilungamo, ndi mitundu ya anthu ndi coonadi.
—Masalmo 96.13

**Maso a Yehova ali ponseponse,
nayang'anira oipa ndi abwino.**

—Miyambo 15.3

**Munandisanthula, Yehova, ni-
mundidziwa. Inu mudziwa ku-
khala kwanga ndi kuuka kwanga,
muzindikira lingaliro langa muli
kutali. Muyesa popita ine ndi po-
goni ine, ndi njira zanga zonse
muzolowerana nazo. Pakuti asa-
nafike mau pa lilime langa, tao-
nani, Yehova, muwadziwa onse.**

—Masalmo 139.1-4

**... Pakuti Yehova saona monga
aona munthu; pakuti munthu aya-
ng'ana cooneka ndi maso, koma
Yehova ayang'ana mumtima.**

—1 Samueli 16.7

**Kodi Iye wakupanga khutu
ngwosamva? Kodi Iye wakuumba
diso ngwosapenya? —Masalmo 94.9**

**Pakuti maso anga ali pa njira
zao zonse, sabisika pa nkhope
yanga, mphulupulu yao siibisika
pamaso panga. —Yeremiya 16.17**

**Ndipo palibe colengedwa cosao-
nekeri pamaso pace, koma zonse
zikhala za pambalambanda ndi
zobvundukuka pamaso pace pa I-
ye amene ticita naye. —Ahebri 4.13**

**Pakuti maso ace ali pa njira ya
munthu ali yense, napenya mo-
ponda mwace monse. Palibe mdi-
ma kapena mthunzi wa imfa, kuti
ocita zopanda pace abisaleko.**

—Yobu 34.21, 22

18 Kutembenuka kusiya machimo ndikofunikira

Ngati ndikondwera nayo imfa ya woipa? ati Ambuye Yehova, si ndiko kuti abwerere kuleka njira yace, ndi kukhala ndi moyo?

—Ezekieli 18.23

Ndinena kwa inu, Iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo.

—Luka 13.3

Wobisa macimo ace sadzaona mwai; koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacitidwa cifundo.

—Miyambo 28.13

Koma ngakhale tsopano, ati Yehova, munditembenukire Ine ndi mtima wanu wonse, ndi kusala,

ndi kulira, ndi kucita maliro; ndipo ng'ambani mitima yanu, si zobvala zanu ai; ndi kutembenukira kwa Yehova Mulungu wanu; pakuti Iye ndiye wacisomo, ndi wozala cifundo, wosapsa mtima msanga, ndi wocuruka kukoma mtima

—Yoweli 2.12, 13

Mukani nao mau, nimubwerere kwa Yehova; nenani kwa Iye, Cotsani mphulupulu zonse, nimulandire cokoma

—Hoseya 14.2

Apenyerera anthu, ndi kuti, Ndinacimwa Koma anandiombola ndingatsikire kumanda, ndi moyo wanga udzaona kuunika.

—Yobu 33.27, 28

Funani Yehova popezeka Iye, i-tanani Iye pamene ali pafupi; wo-ipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama asiye maganizo ace, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamcitira cifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adza-khululukira koposa. —Yesaya 55.6, 7

Yehova ali pafupi ndi iwo a mti-ma wosweka, apulumutsa iwo a mzimu wolapadi. —Masalmo 34.18

... Kuti abwerere yense kuleka njira yace yoipa; kuti ndikhululukire ... cimo lao. —Yeremiya 36.3

Ndinabvomera coipa canga kwa Inu; ndipo mphulupulu yanga sindinaibisa. Ndinati, Ndidzaululira Yehova macimo anga; ndipo

munakhululukira coipa ca kula-kwa kwanga. —Masalmo 32.5

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. —1 Yohane 1.9

Cifukwa cace lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu. . . . —Macitidwe a atumwi 3.19

Cifukwa cace lapa coipa cako ici, pemphera Ambuye, kuti kape-na akukhululukire iwe colingirira ca mtima wako.

—Macitidwe a atumwi 8.22

Kulapa ndiko kusiya uchimo ndi kuu-vomereza pamaso pa Mulungu.

20 Nsembe yofunikira kutiyanjanitsa kwa Mulungu

(Uchimo udabweretsa kulekanitsidwa, tsamba 14.)

Pakuti moyo wa nyama ukhala m'mwazi; ndipo ndakupatsani uwu pa guwa la nsembe, ucite cotetezera moyo wanu; pakuti wocita cotetezera ndiwo mwazi, cifukwa ca moyo wace. —Levitiko 17.11

Mwana wa nkhusa wanu azikhala wangwiro, wamwamuna, wa ca ka cimodzi Ndipo mwaziwo udzakhala cizindikilo kwa inu pa nyumba zimene mukhalamo; pamene ndiona mwaziwo ndidzapitirira inu, ndipo sipadzakhala mliri wakukuonongani

—Eksodo 12.5, 13

Ndipo monga mwa cilamulo zitsala zinthu pang'ono zosayeretsedwa ndi mwazi, ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka.

—Ahebri 9.22

Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzadzifunira yekha mwana wa nkhusa wa nsembe yopsereza Ndipo Abrahamu anatukula maso ace nayang'ana taonani, pambuyo pace nkhusa yamphongo yogwiridwa ndi nyanga zace m'ciyangoyangomo; ndipo ananka Abrahamu nakatenga nkhusa yamphongoyo, naipereka nsembe yopsereza m'malo mwa mwana wace. —Genesis 22.8, 13

Yesu ndiye Mwana wa nkhosa woperekedwa ndi Mulungu

21

M'mawa mwace anaona Yesu alinkudza kwa iye, nanena, Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene acotsa cimo lace la dziko lapasi!
—Yohane 1.29

Iye anatsenderezedwa koma anadzicepetsa yekha osatsegula pakamwa pace; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa
—Yesaya 53.7

Kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa Iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo ciombolo cosatha. Kote-ro Kristunso ataperekedwa nse-

mbe kamodzi kukasenza macimo a ambiri
—Ahebri 9.12, 28

Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zobvunda, golidi ndi siliva, . . . koma ndi mwazi wa mtengo wace wapatali monga wa mwana wa nkhosa wopanda cirema, ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Kristu.
—1 Petro 1.18, 19

Koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungu mwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyantsa ndi nchito zakufa, kukatunkira Mulungu wamoyo?

—Ahebri 9.14

22 Chipulumutso chaperekedwa ndi Mulungu yekha

Ndipo ayesedwa olungama kwaulere, ndi cisomo cace, mwa ciombolo ca mwa Kristu Yesu; amene Mulungu anamuika poyera akhale cotetezera mwa cikhulupiriro ca m'mwazi wace . . .

—Aroma 3.24, 25

Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife. Ndipo tsono popeza inayesedwa olungama ndi mwazi wace, makamaka ndithu tidzapulumuka mkwiyo wa Mulungu mwa Iyeyo.

—Aroma 5.8, 9

Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa nchito ya

lamulo, koma mwa cikhulupiriro ca Yesu Kristu . . .

—Agalatiya 2.16

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, . . . ciri mphatso ya Mulungu.

—Aefeso 2.8

Ameneyu aneneri onse amcitira umboni, kuti onse akumkhulupirira Iye adzalandira cikhululukiro ca macimo ao, mwa dzina lace.

—Macitidwe a atumwi 10.43

Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, lime ne tiyenera kupulumutsidwa nalo.

—Macitidwe a atumwi 4.12

...Mngelo Gabrieli anatumi-dwa ndi Mulungu kunka ku mudzi wa ku Galileya dzina lace Nazarete, kwa namwali wopalidwa ubwenzi ndi mwamuna, dzina lace Yosefe, wa pfuko la Davide; ndipo dzina lace la namwaliyo ndilo Mariya. . . . Ndipo mngelo anati kwa iye, Usaope, Mariya; pakuti wapeza cisomo ndi Mulungu. Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamucha dzina lace Yesu. Iye adzakhala wamkuru, nadzachedwa Mwana wa Wamkurukuru: . . . ndipo ufumu wace sudzatha. Koma Mariya anati kwa mngelo, Ici cidzacitika bwanji, popeza ine

sindidziwa mwamuna? Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe: cifukwa cace-nso Coyeraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu. . . .Cifukwa palibe mau amodzi akucokera kwa Mulungu adzakhalapanda mphamvu. Ndipo Mariya anati, . . . kukhale kwa ine monga mwa mau anu. . . . —Luka 1.26-38

Anthu awiri wokha amene adabwera mdziko wopanda Mwamuna ndi Mkazi kukhalira pamodzi ndi Adamu ndi Kristu. Adamu adabweretsa uchimo mdziko, Koma Yesu adabweretsa chigonjetso pa, uchimo.

Ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanaciyesa colanda kukhala wofana ndi Mulungu, ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha, nakhala womvera kufikirira imfa —Afilipi 2.6, 8

Ine ndi Atate ndife amodzi. Kodi inu munena za Iye, amene Atate anampatula namtuma ku dziko lapansi, Ucita mwano; cifukwa ndinati, Ndiri Mwana wa Mulungu? —Yohane 10.30, 36

Yesu Kristu, Mawu amyaya, anakhala ndi moyo nthawi zonse. Mwa machitidwe a mphamvu Mulungu anampanga kuti akayimikidwe m'mimba mwa Maria. Kuthupi amadziwika monga Mwana

wa Munthu, ndipo ku uzimu ndi Mwana wa Mulungu. Malemba amagwiritsa ntchito liwu lakuti “Mwana” pofuna ku-longosoa chiyanjano chimene chilipo pakati pa Mulungu ndi Mawu ake—Yesu Kristu.

Mwa ici polowa m'dziko lapansi, anena, . . . Koma thupi muna-ndikonzera Ine. —Ahebri 10.5

Amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa ciyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Kristu Ambuye wathu.

—Aroma 1.4

Tomasi anayankha nati kwa Iye, Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga. —Yohane 20.28

Ndipo pobvomerezeka, cinsinsi ca kucitira Mulungu ulemu ncacikuru: Iye amene anaonekera m'thupi —1 Timoteo 3.16

**Pakuti mwa Iye cikhalira cidzalo ca Umulungu m'thupi.
—Akolose 2.9**

Pakuti kwa ife mwana wakhandabwitsa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lace, ndipo adzamucha dzina lace Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa mtendere. —Yesaya 9.6

Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye mu-

nthu, Kristu Yesu, amene anadzipereka yekha ciombolo m'malo mwa onse —1 Timoteo 2.5, 6

Yesu anati kwa iwo, . . . asanyambe kukhala Abrahamu ndipo Ine ndiripo. —Yohane 8.58

**Mwa Iye munali moyo; ndi moyowu unali kuunika kwa anthu. Anali m'dziko lapansi, ndi dziko linalengedwa ndi Iye, koma dziko silinamzindikira Iye.
—Yohane 1.4, 10**

**Amene tiri nao maomboledwe mwa Iye, m'kukhululukidwa kwa zocimwa zathu; amene ali fanizo la Mulungu wosaonekayo
—Akolose 1.14, 15**

26 Baibulo (Malembo Woyera) ndilo Mawu a Mulungu

**Pakuti kale lonse cinenero sici-
nadza ndi cifuniro ca munthu; ko-
ma anthu a Mulungu, ogwidwa
ndi Mzimu Woyera, analankhula.**

—2 Petro 1.21

**Monga Iye analankhula ndi
m'kamwa mwa aneneri ace oyera
mtima, a kale lomwe Kuwapa-
tsa anthu ace adziwitse cipulu-
mutso, ndi makhululukidwe a ma-
cimo ao.**

—Luka 1.70, 77

**Mzimu wa Yehova unalankhula
mwa ine, ndi mau ace anali pa lili-
me langa.**

—2 Samueli 23.2

**Ndipo mau awa ndikuuzani lero,
azikhala pamtima panu.**

—Deuteronomo 6.6

**Lemba liri lonse adaliuzira Mu-
lungu, ndipo lipindulitsa pa ci-
phunzitso, citsutsano, cikonzero,
cilangizo ca m'cilungamo.**

—2 Timoteo 3.16

**Pakuti zonse zinalembedwa
kale zinalembedwa kutilangiza,
kuti mwa cipiriro ndi citonthozo
ca malembo, tikhale ndi ciyembe-
kezo.**

—Aroma 15.4

**. . . Mungolakwa osadziwa male-
mbo, kapena mphamvu za Mulu-
ngu.**

—Mateyu 22.29

**. . . Popeza munakuzitsa mau
anu koposa dzina lanu lonse.**

—Masalmo 138.2

Ndipo abvala cobvala cowazi-dwa mwazi; ndipo achedwa dzina lace, Mau a Mulungu.

—Cibvumbulutso 19.13

Paciyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife —Yohane 1.1, 14

Yesu amavumbulutsa Mulungu

Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa ciwalitsiro ca cidziwitso ca ulemmerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Kristu. —2 Akorinto 4.6

Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; Mwana woba-dwa yekha wakukhala pa cifuwa ca Atate, Iyeyu anafotokozera.

—Yohane 1.18

Mulungu amalankhula kupyolera mwa Yesu

Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manene-dwe ambiri ndi mosiyana-siyana, koma pakutha pace pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe. —Ahebri 1.1, 2

Zimene ndinaona Ine kwa Atate, ndilankhula —Yohane 8.38

28 Mawu olembedwa ndi Mawu Amoyo alinganizidwa

Baibulo ndi chakudya cha moyo

... Ndasungitsa mau a pakamwa pace koposa lamulo langa langa.
—Yobu 23.12

... Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m'kamwa mwa Mulungu.
—Mateyu 4.4

Baibulo limaunikira pa njira yathu

Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga.
—Masalmo 119.105

Potsegulira mau anu paunikira; kuzindikiritsa opusa.
—Masalmo 119.130

Yesu ndiye Mkate wochokera kumwamba

Mkate wamoyo wotsika Kumwamba Ndine amene. Ngati munthu wina akadyako mkate umene, adzakhala ndi moyo kosatha. Inde, ndipo mkate umene ndidzapatsa Ine, ndiwo thupi langa, ukhale moyo wa dziko lapansi.
—Yohane 6.51

Yesu ndiye kuunika kwa dziko lapansi

Pamenepo Yesu analankhulanso nao, nanena, Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata Ine sadzayenda mumdima, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo.
—Yohane 8.12

**Baibulo limabweretsa moyo
wobala zipatso**

Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; ndipo m'cilamulo cace amalingirira usana ndi usiku. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace —Masalmo 1.2, 3

**Yesu amapatsa moyo 29
wobala zipatso**

Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. . . . Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zace: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu. —Yohane 15.4, 5

Malemba amakamba za Yesu Kristu

Musanthula m'malembo, popeza muyesa kuti momwemo muli nao moyo wosatha; ndipo akundicitira Ine umboni ndi iwo omwe wo Pakuti mukadakhulupirira Mose, mukadakhulupirira Ine; pakuti iyeyu analembera za Ine. —Yohane 5.39, 46

Ndipo anayamba kwa Mose, ndi kwa aneneri onse, nawatanthauzira iwo m'malembo onse zinthu za Iye yekha. —Luka 24.27

Ndipo Filipino anatsegula pakamwa pace, nayamba pa lembo ili, nalalikira kwa iye Yesu. —Macitidwe a atumwi 8.35

Mau anu aikika kumwamba, kosatha, Yehova. Ciwerengero ca mau anu ndico coonadi; ndi maweruzo anu olungama onse akhala kosatha. —Masalmo 119.89, 160

Udzu unyala, duwa lifota, koma mau a Mulungu wathu adzakhala nthawi zacikhalire. —Yesaya 40.8

... Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kace kamodzi sikadzacokera kucilamulo, kufikira zitacididwa zonse.

—Mateyu 5.18

... Ndipo colemba sicingathe kutyoka. —Yohane 10.35

Munthu asayese kusintha Baibulo

Ciri conse ndikuuzani, mucisamalire kucicita; musamaonjezako, kapena kucepsako.

—Deuteronomo 12.32

Usaonjezere kanthu pa mau ace, angakudzudzule, nungatsutsidwe kuti ulikunama. —Miyambo 30.6

Ndipo ali yense akacotsako pa mau a buku la cinenero ici, Mulungu adzamcotsera gawo lace pa mtengo wa moyo

—Cibvumbulutso 22.19

Wonyoza mau adziononga yekha —Miyambo 13.13

Imfa ya Yesu inakwaniritsa chikonzero cha Mulungu 31

Cifukwa ca ici Atate andikonda Ine, cifukwa nditaya Ine moyo wanga, kuti ndikautengenso. Pali be wina andicotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu yakuutaya, ndi mphamvu ndiri nayo yakuutenganso. . . .

—Yohane 10.17, 18

Yesu anamyankha iye, Simukadakhala nao ulamuliro uli wonse pa Ine, ngati sukadapatsidwa kwa inu kucokera Kumwamba

—Yohane 19.11

Kapena uganiza kuti sindinga the kupemphera Atate wanga, ndipo Iye adzanditumizira tsopano lino mabungwe a angelo oposa khumi ndi awiri? Koma pakutero

malembo adzakwaniridwa bwanji, pakuti kuyenera comweco?

—Mateyu 26.53, 54

Koma zimene Mulungu analalikiratu m'kamwa mwa aneneri onse, kuti adzamva kuwawa Kristu, Iye anakwaniritsa coteru.

—Macitidwe a atumwi 3.18

Ameneyo, woperekedwa ndi uphungu woikidwa ndi kudziwiratu kwa Mulungu, inu mwampacika ndi kumupha ndi manja a anthu osayeruzika.

—Macitidwe a atumwi 2.23

Koma kunakomera Yehova kumtundudza; anammvetsa zowa wa; moyo wace ukapereka nsembe yoparamula —Yesaya 53.10

Ndipo anapacika pamodzi ndi Iye acifwamba awiri; mmodzi ku dzanja lace lamanja ndi wina kula-manzere. . . . Ndipo iwo akupacikidwa naye anamlalatira.

—Marko 15.27, 32

Cifukwa cace anadza asilikari natyola miyendo ya woyambayo, ndi ya winayo wopacikidwa pamodzi ndi Iye; koma pofika kwa Yesu, m'mene anamuona Iye, kuti wafa kale, sanatyola miyendo yace; koma mmodzi wa asilikari anamgwaza ndi nthungo m'nthiti yace, ndipo panaturuka pomwepo mwazi ndi madzi. . . . Pakuti izi zinacitika, kuti lembo likwaniridwe,

Pfupa la Iye silidzatyoledwa. Ndipo . . . Adzayang'ana pa Iye amene anampyoza. —Yohane 19.32-37

Ndipo ora lacisanu ndi cimodzi panali mdima pa dziko lonse, kufikira ora lacisanu ndi cinai. . . . Ndipo Yesu, pamene anapfula ndi mau akuru, anapereka mzimu wace. . . . Ndipo dziko lina-gwedezeke, ndi miyala inang'ambika. Ndipo pamene mkuru wa asilikari, ndi iwo anali naye akudikira Yesu, anaona cibvomezi, ndi zinthu zimene zinacitidwa, anao-pa kwambiri, nanena, Indedi Uyo ndiye Mwana wa Mulungu.

—Mateyu 27.45, 50-51, 54

Yemweyo Mulungu anamuukitsa, atamasula zowawa za imfa, mwakuti sikunali kotheka kuti Iye agwidwe nayo. Yesu ameneyo, Mulungu anamuukitsa; za ici tiri mboni ife tonse.

—Macitidwe a atumwi 2.24, 32

Popeza tsono ana ndiwo a mwa-zi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nao makhalidwe omwe-wo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi; nakamasule iwo onse amene, cifukwa ca kuopa imfa, m'moyo wao wonse adamangidwa ukapolo.

—Ahebri 2.14, 15

Imfawe, cigonjetso cako ciri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti? Koma ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife cigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Kristu.

—1 Akorinto 15.55, 57

Ndi Wamoyoyo; ndipo ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade.

—Cibvumbulutso 1.18

Koma caonetsedwa tsopano m'maonekedwe a Mpulumutsi wathu Kristu Yesu, amenedi anatha imfa, naonetsera poyera moyo ndi cosabvunda mwa Uthenga Wabwino.

—2 Timoteo 1.10

Taona, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine. —Cibvumbulutso 3.20

Koma kwa iye amene sacita, koma akhulupirira Iye amene ayesa osapembedza ngati olungama, cikhulupiro cace ciwerengedwa cilungamo. —Aroma 4.5

... Landirani Mzimu Woyera. ... Pemphani, ndipo mudzalandira, kuti cimwemwe canu cikwani-ridwe. —Yohane 20.22; 16.24

Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima

mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka.

—Aroma 10.9

Iye wakukonda atate wace, kapena amace koposa Ine, sayenera Ine Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. Pakuti iye amene afuna kupulumutsa moyo wace adzautaya: koma iye amene ataya moyo wace cifukwa ca Ine, adzaupenza. —Mateyu 10.37; 16.24, 25

Koma ngati muli a Kristu, muli mbeu ya Abrahamu, nyumba monga mwa lonjezano.

—Agalatiya 3.29

... Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wace. Iye wakhala ndi Mwana ali nao moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo. —1 Yohane 5.11, 12

Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimacula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa. —Aroma 8.2

Koma Mulungu, wolemera cifundo, ... tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Kristu (muli opulumutsidwa ndi cisomo).

—Aefeso 2.4, 5

Ndinapacikidwa ndi Kristu; koma ndiri ndi moyo; wosatinso ine

ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao tsopano m'thupi, ndiri nao m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu —Agalatiya 2.20

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolegedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano. —2 Akorinto 5.17

Inu amene mudabadwanso, osati ndi mbeu yofeka, komatu yosola, mwa mau a Mulungu amoyo ndi okhalitsa. Lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda cinyengo, kuti mukakule nao kufikira cipulumutso.

—1 Petro 1.23; 2.2

Mulungu, mokhala mwace moyera, ndiye Atate wa ana amasiye, ndi woweruza wa akazi amasiye.

—Masalmo 68.5

Koma tsopano, Yehova, Inu ndinu Atate wathu; ife tiri dongo, ndipo Inu ndinu Muumbi wathu; ndipo ife tonse tiri nchito ya dzanja lanu.... Inu Yehova ndinu Atate wathu, Mombolo wathu wakikhalire ndi dzina lanu.

—Yesaya 64.8; 63.16

... Ndipo kudzatero kuti m'mene adawanena, Simuli anthu anga, adzanena nao, Muli ana a Mulungu wamoyo.

—Hoseya 1.10

Comweco, ngati inu, muli oipa, mudziwa kupatsa ana anu mpha-

tso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akumpempha Iye? ... Cifukwa cace pempherani inu comweci: Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe.

—Mateyu 7.11; 6.9

... Ndipo Ine ndidzalandira inu, ndipo ndidzakhala kwa inu Atate, ndi inu mudzakhala kwa Ine ana amuna ndi akazi, anena Ambuye Wamphamvuyonse.

—2 Akorinto 6.17, 18

Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu.

—Aroma 8.14

Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Pali be munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine. Mukadazindikira Ine mukadadziwa Atate wanganso; kuyambira tsopano mumzindikira Iye, ndipo mwamuona Iye... Ngati wina akonda Ine, adzasungana mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo. —Yohane 14.6, 7, 23

...Mulungu anatuma Mwana wace, ...kuti ife tikalandire umwana. Ndipo popeza muli ana, Mulungu anatumiza Mzimu wa Mwana wace alowe m'mitima yathu, wopfuula Abba, Atate. Kote-

ro kuti sulinso kapolo, koma mwana; koma ngati mwana, wolowa nyumbanso mwa Mulungu. Pakuti inu nonse muli ana a Mulungu, mwa cikhulupiro ca mwa Yesu Kristu. —Agalatiya 4.4-7; 3.26

Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace. —Yohane 1.12

...Ndipo akacimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Kristu wolungama.

—1 Yohane 2.1

Kuti mwa Iye ife tonse awiri tiri nao malowedwe athu kwa Atate, mwa Mzimu mmodzi. —Aefeso 2.18

38 Yesu amabweretsa chikondi, chimwemwe, mtendere

... Mulungu ndiye cikondi, ndipo iye amene akhala m'cikondi akhala mwa Mulungu, ndipo Mulungu akhala mwa iye. —1 Yohane 4.16

Koma mukhalirane okoma wina ndi mnzace, a mtima wacifundo, akukhululukirana nokha, monga nso Mulungu mwa Kristu anakhululukira inu. —Aefeso 4.32

Mwa ici adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli naco cikondano wina ndi mnzace. —Yohane 13.35

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere. . . . —Agalatiya 5.22

Koma ndidzakondwera mwa Yehova, ndidzasekerera mwa Mulu-

ngu wa cipulumutso canga.

—Habakuku 3.18

Mudzandidziwitsa njira ya moyo: pankhope panu pali cimwemwe cokwanira; m'dzanja lanu lamanja muli zokondweretsa zomka muyaya. —Masalmo 16.11

Popeza tsono tayeredwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu.

—Aroma 5.1

Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dzi-ko lapansi lipatsa. Mtima wanu usabvutike, kapena usacite mantha. —Yohane 14.27

Koma ngati Mzimu wa Iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, Iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakhala mwa inu. —Aroma 8.11

Koma Mulungu anaukitsa Ambuye, ndiponso adzaukitsa ife mwa mphamvu yace.
—1 Akorinto 6.14

Pakuti cifuniro ca Atate wanga ndi ici, kuti yense wakuyang'ana Mwana, ndi kukhulupirira Iye, akhale nao moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lo-mariza.
—Yohane 6.40

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo: wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo. —Yohane 11.25

Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso mwa munthu. Pakuti monga mwa Adamu onse amwalira, coteronso mwa Kristu onse akhalitsidwa ndi moyo. Koma yense m'dongosolo lace la iye yekha, cipatso coundukula Kristu; pomwepo iwo a Kristu, pa kubwera kwace. —1 Akorinto 15.21-23

... Popeza Ine ndiri ndi moyo inunso mudzakhala ndi moyo.
—Yohane 14.19

40 Musalekelere chipulumutso chachikulu chotere

Munthu wopeputsa cilamulo ca Mose angofa opanda cifundo pa mboni ziwiri kapena zitatu: ndipo mutani, kulanga koposa kotani nanga adzayesedwa woyenera iye amene anapondereza Mwana wa Mulungu, nayesa mwazi wa cipangano umene anayeretsedwa nao cinthu wamba, nacidira cipongwe Mzimu wa cisomo. —Ahebri 10.28, 29

Iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mau anga, ali naye womweruza iye; mau amene ndalankhula, iwowa adzamweruza tsiku lomariza. —Yohane 12.48

Cifukwa cace ndinati kwa inu, kuti mudzafa m'macimo anu, pakuti ngati simukhulupirira kuti

Ine ndine, mudzafa m'macimo anu. —Yohane 8.24

Ndipo ndinena kwa inu, abwenzi anga, Musaope iwo akupha thupi, ndipo akatha ici alibe kanthu kena angathe kucita. Koma ndidzakulangizani amene muzimuopa; taopani Iye amene atatha kupha ali ndi mphamvu yakutaya kugehena, inde, ndinena ndinu opani ameneyo. —Luka 12.4, 5

Tidzapulumuka bwanji ife, tika-panda kusamala cipulumutso cacikuru coteru? —Ahebri 2.3

... Koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye. —Yohane 3:36

Cifukwa anapangira tsiku lime-
ne adzaweruza dziko lokhalamo
anthu m'cilungamo, ndi munthu
amene anamuikiratu; napatsa
anthu onse citsimikizo, pamene
anamuukitsa Iye kwa akufa.

—Macitidwe a atumwi 17.31

Pakuti Atate saweruza munthu
ali yense, koma anapereka kuwe-
ruza konse kwa Mwana; kuti onse
akalemekeze Mwana, monga ale-
mekeza Atate. . . . —Yohane 5.22, 23

. . . Pa bvumbulutso la Ambuye
Yesu wocokera Kumwamba pa-
modzi ndi angelo a mphamvu ya-
ce, m'lawi lamoto, ndi kubwezera
cilango kwa iwo osamdziwa Mulu-

ngu, ndi iwo osamvera Uthenga
Wabwino wa Ambuye wathu Yesu.

—2 Atesalonika 1.7, 8

Tsiku limene Mulungu adzawe-
ruza ndi Yesu Kristu zinsinsi za
anthu

—Aroma 2.16

Pakuti ife tonse tiyenera kuo-
netsedwa ku mpando wa kuweru-
za wa Kristu, kuti yense alandire
. . . monga momwe anacita, kape-
na cabwino kapena coipa.

—2 Akorinto 5.10

Koma adani anga aja osafuna
kuti ndidzakhala mfumu yao,
bwerani nao kuno, nimuwaphe pa-
maso panga.

—Luka 19.27

Abvomereza kuti adziwa Mulungu, koma ndi nchito zao amkana Iye, popeza ali onyansitsa, ndi osamvera, ndi pa nchito zonse zabwino osatsimikizidwa. —Tito 1.16

... Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu. —Aroma 8.9

... Nakhala pansi pamaso pako ngati anthu anga, namva mau ako, koma osawacita; pakuti pakamwa pao anena mwacikondi, koma mtima wao utsata phindu lao. —Ezekieli 33.31

Anthu awa andilemekeza Ine ndi milomo yao; koma mtima wao uli kutari ndi Ine. —Mateyu 15.8

Comweco inunso muonekera o-

lungama pamaso pa anthu, koma m'kati muli odzala ndi cinyengo ndi kusayeruzika. —Mateyu 23.28

Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidza-fukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika.

—Mateyu 7.21-23

Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira Iye, ngati tisunga malamulo ace.
—1 Yohane 2.3

Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzalinga maweruzo anga ndi kuwacita.
—Ezekieli 36.27

Ndipo pamene anakonzeka wamphumphu anakhala kwa onse akumvera Iye cifukwa ca cipulumutso cosatha.
—Ahebri 5.9

Ndipo pamene munamasulidwa kuucimo, munakhala akapolo a cilungamo.
—Aroma 6.18

Pakuti ife ndife cipango cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulu-

ngu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo.
—Aefeso 2.10

Ndipo ngati Kristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa cifukwa ca ucimo; koma mzimu uli wamoyo cifukwa ca cilungamo. Pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zocita zace za thupi, mudzakhala ndi moyo.
—Aroma 8.10, 13

... Adzipatule kwa cosalungama yense wakuchula dzina la Ambuye.
—2 Timoteo 2.19

Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu.

—Macitidwe a atumwi 5.29

Ngati dziko lapansi lida inu, mudziwa kuti lidada Ine lisanyambe kuda inu. Mukadakhala a dziko lapansi, dziko lapansi likadakonda zace za lokha; koma popeza simuli a dziko lapansi, koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi, cifukwa ca ici likudani inu. —Yohane 15.18, 19

... Koma ikudza nthawi imene yense wakupha inu adzayesa kuti atumikira Mulungu. Ndipo izi adzacita, cifukwa sanadziwa Atate, kapena Ine. —Yohane 16.2, 3

Taonani, cikondico Atate watipatsa, kuti tichedwe ana a Mulungu; ndipo tiri ite otere. Mwa ici dziko lapansi silizindikira ife, po-

peza silimzindikira Iye.

—1 Yohane 3.1

... Ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri.

—Macitidwe a atumwi 14.22

Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo.

—2 Timoteo 3.12

Ine ndawapatsa iwo mau anu; ndipo dziko lapansi linadana nao, cifukwa sakhala a dziko lapansi, monga Ine sindikhala wa dziko lapansi. ... M'dziko lapansi mudzakhala naco cibvuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine. —Yohane 17.14; 16.33

Ndi kutaya pa Iye nkhwawa yanu yonse, pakuti Iye asamalira inu.

—1 Petro 5.7

Usaope, pakuti Ine ndiri pamo-dzi ndi iwe; usaopsyedwe, pakuti Ine ndine Mulungu wako; ndidza-kulimbitsa; inde, ndidzakutha-ngata; inde, ndidzakucirikiza ndi dzanja langa lamanja la cilunga-mo.

—Yesaya 41.10

Pakuti wandisiya atate wanga ndi amai wanga, koma Yehova anditola.

—Masalmo 27.10

Kotero kuti tinena molimbika mtima, Mthandizi wanga ndiye Ambuye; sindidzaopa; adzandici-tira ciani munthu?

—Ahebri 13.6

Mukatonzedwa pa dzina la Kri-stu, odala inu; pakuti Mzimu wa ulemerero, ndi Mzimu wa Mulu-ngu apuma pa inu.

—1 Petro 4.14

Pakuti adzalamulira angelo ace za iwe, akusunge m'njira zako zo-nse. Inde, ndingakhale ndiyenda m'cigwa ca mthunzi wa imfa, si-ndidzaopa coipa; pakuti Inu muli ndi ine: cibonga canu ndi ndodo yanu, izi zindisangalatsa ine.

—Masalmo 91.11; 23.4

Ndikhoza zonse mwa Iye wondi-patsa mphamvuyo. Koma Mulu-ngu wanga adzakwaniritsa coso-wa canu ciri conse monga mwa cu-ma cace m'ulemerero mwa Kristu Yesu.

—Afilipi 4.13, 19

Sicinakugwerani inu ciyeso koma ca umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalo la inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi ciyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako.

—1 Akorinto 10.13

Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wacifumu waciso-mo, kuti tilandire cifundo ndi kupenza cisomo ca kutithandiza nthawi yakusowa.

—Ahebri 4.16

Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzace, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambi-

tsa kuticotsera ucimo wonse.

—1 Yohane 1.7

Koma thawa zilakolako za unyamata, nutsate cilungamo, cikhulupiro, cikondi, mtendere, pamodzi ndi iwo akuitana pa Ambuye ndi mitima yoyera.

—2 Timoteo 2.22

Cotero inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu.

—Aroma 6.11

Potero mverani Mulungu; koma kanizani mdierekezi, ndipo adzakuthawani inu.

—Yakobo 4.7

Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire Inu.

—Masalmo 119.11

Pamene munati, Funani nkhope yanga; mtima wanga unati kwa Inu: Nkhope yanu, Yehova, ndidzaifuna. —Masalmo 27.8

Khulupirani pa Iye nyengo zonse, anthu inu: tsanulirani mitima yanu pamaso pace: Mulungu ndiye pothawirapo ife. —Masalmo 62.8

Mundiciritse ine, Yehova, ndipo ndidzaciritsidwa; mundipulumutse ine, ndipo ndidzapulumutsidwa; pakuti cilemekezo canga ndinu. —Yeremiya 17.14

Pempherani kosaleka; m'zonse yamikani; pakuti ici ndi cifuniro ca Mulungu ca kwa inu, mwa Kristu Yesu. —1 Atesalonika 5.17, 18

Koma wina wa inu ikamsowa

nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye. —Yakobo 1.5

Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhala mwa inu, pemphani cimene ciri conse mucifuna ndipo cidzacitika kwa inu.

—Yohane 15.7

Ndinafuna Yehova ndipo anandibvomera, nandilanditsa m'mantha anga onse. —Masalmo 34.4

Ndikadasekera zopanda pace m'mtima mwanga, Ambuye saka-damvera. Cifukwa ca dzina lanu, Yehova, ndikhululukireni kusakaza kwanga, pakuti ndiko kwakukuru. —Masalmo 66.18; 25.11

Pakuti Ambuye adzatsika Ku-mwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.

—1 Atesalonika 4.16, 17

Ndipo tsopano, tiana, khalani mwa Iye; kuti akaonekere Iye tikakhale nako kulimbika mtima, osacita manyazi kwa Iye pa kudza kwace.

—1 Yohane 2.28

Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okondedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsiriza ciyero m'kuopa Mulungu.

—2 Akorinto 7.1

Lezani mtima inunso, limbitsani mitima yanu; pakuti kudza kwace kwa Ambuye kuyandikira. Musaipidwe wina ndi mnzace, abale, kuti mungaweruzidwe. Taonani, woweruza aima pakhomo.

—Yakobo 5.8, 9

Khalani okonzeka inunso; cifu kwa nthawi imene simulingirira, Mwana wa munthu akudza.

—Luka 12.40

Dzazidwani ndi Mzimu wa Mulungu

Tembenukani pamene ndikudzudzulani; taonani, nditsanulira pa inu mzimu wanga, ndikudziwitsani mau anga. —Miyambo 1.23

... Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu ku-loza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

—Macitidwe a atumwi 2.38

Ndipo musaledzere naye vinyo, m'mene muli citayiko; komatu mudzale naye Mzimu, ndi kudzi-lankhulira nokha ndi masalmo, ndi mayamiko, ndi nyimbo zauzimu, kuyimbira ndi kuyimba m'malimba Ambuye mumtima mwanu;

ndi kuyamika Mulungu Atate masiku onse, cifukwa ca zonse, m'dzina la Ambuye wathu Yesu Kristu; ndi kumverana wina ndi mnzace m'kuopa Kristu.

—Aefeso 5.18-21

Pakuti wakucita mwa inu kufuna ndi kucita komwe, cifukwa ca kukoma mtima kwace, ndiye Mulungu.

—Afilipi 2.13

Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu.

—1 Akorinto 3.16; 6.20

Scripture text reprinted from the Bible in Chichewa by permission of United Bible Societies Africa Regional Centre, Nairobi, Kenya.

Published in numerous languages by World Missionary Press, Inc., as God supplies funds in answer to prayer. **For questions or more information by country, visit: www.wmp-contacts.org**

Bukhuli ndi laulere — Siligulitsidwa

World Missionary Press
PO Box 120
New Paris, IN 46553-0120 USA
www.wmpress.org

6/23



Read booklets online or by App
www.wmp-readonline.org

1526 Chichewa HKG